Muziona Moyo Ngati Mmene Mulungu Amauonera

(Gawo 1)

Nkhaniyi yachokera m'mutu 13 wa buku lakuti, *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* lomwe likupezeka pa jw.org/ny.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso zifukwa zake. Fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa, kenako ganizirani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.

KODI MULUNGU AMAKHUDZIDWA BWANJI NDI MMENE INUYO MUMAONERA MOYO?

1 GANIZIRANI MOZAMA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

Kodi anthu ena anganene kuti chiyani?

_____

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

_____

_____

Nanga n'chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

_____

_____

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Moyo ndi mphatso yochokera kwa Mulungu.

(Werengani mutu 13 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 1 ndi 2.)

Werengani Chivumbulutso 4:11.

Kodi lembali likusonyeza kuti n'chifukwa chiyani tiyenera kulemekeza Mulungu?

Werengani Machitidwe 14:16, 17.

Kodi Yehova amasamalira bwanji moyo?

Anthu amayesetsa kusamalira zinthu zimene amaziona kuti ndi zofunika, nafenso tiyenera kulemekeza mphatso ya moyo

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Zochita zathu ziyenera kusonyeza kuti timalemekeza moyo.

(Werengani mutu 13 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 3 mpaka 9.)

Werengani Ekisodo 21:22, 23; Deuteronomo 5:17 ndi Salimo 127:3.

Kodi mavesiwa amasonyeza bwanji mmene Mulungu amaonera kuchotsa mimba komanso kupha munthu?

Werengani Aroma 12:1 ndi 2 Akorinto 7:1.

Kodi tingasonyeze bwanji kuti timalemekeza moyo?

N'chifukwa chiyani mumaona kuti mphatso ya moyo ndi yofunika?

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

WINA AKANENA KUTI…

Thupi langa ndingachite nalo chilichonse chomwe ndikufuna bola ndisavulaze munthu wina.

MUNGANENE KUTI…

Anthu ambiri angagwirizane ndi mfundo imeneyo. Koma ine ndikuona kuti ndi nzeru kuganizira mmene Mulungu amaonera nkhaniyi chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze zotani kuti munthuyo amvetse bwino lembalo?

_____

WINA AKANENA KUTI…

Munthu akafuna kuchotsa mimba, palibe vuto chifukwa ndi thupi lake.

MUNGANENE KUTI…

N'zoona kuti tonsefe tili ndi ufulu wochita zomwe tikufuna. Koma ndimakhulupirira kuti kuchotsa mimba n'kulakwa chifukwa…

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze zotani kuti munthuyo amvetse bwino lembalo?

_____

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania